**UNDUNA WA ZACHILENGEDWE NDI KUSINTHA KWA NYENGO**

NTHAMBI YOWONA ZANYENGO NDI KUSINTHA KWA NYENGO

**NYENGO MSABATAYI**


**KUYAMBIRA PA 2 MPAKA PA 8 SEPTEMBER, 2024**

## NYENGO M'SABATA IKUBWERAYI

Kuyambira pa Lolemba pa 2 mpaka Lachitatu pa 4 September, 2024 **tiyembekezere nyengo Chiperoni kupitilira, yomwe ndi nyengo yamphepo, yozizira ndi mitambo yochuluka komanso mvula yowaza ndi yamawawa komanso chifunga**. Pa **Nyanja ya Malawi, Chilwa ndi nyanja zina pazikhala mafunde aatali chifukwa cha mphepo yamphamvu ya Mwera yomwe idzachepe mphamvu Lachitatu madzulo.** Nyengoyi ipitilira chifukwa cha mphepo zachinyontho kuchokera kum'mwera chakumvuma kufika ku Malawi. Pali chiyembekezo choti kudzayamba kukhala nyengo yadzuwa ndi yofunda kuyambira Lachinayi mpaka kumathero kwa sabatayi, komabe nyengo yozizira pang'ono idzapitilira usiku ndi m'mawa kamba ka mphepo zofundirapo kuchokera kumvuma.

## NYENGO MU SABATA YANGOTHAYI

M'sabata yathayi kunali kwa mphepo, mitambo komanso nyengo yozizira ndi mvula inagwa yomwe inali yamphamvu m'madera ena. Pa 30 August 2024 mvula yambiri inagwa ku **Nkhande (Ntcheu) yamlingo wa 68 mm**, komanso **Nkhombwe ADMARC (Blantyre) 59.3 mm** ndi **Njolomole Agriculture 52 mm**., Ku Nkhombwe ADMARC (Blantyre) inagwa ya mlingo wa 25.3 mm pa 31 August. Mvula inagwanso yochulukilapo ku Machinga Nyambi ndi 17.5 mm komanso kwa Ngabu 16.6 mm. Pa 1 September 2024 mvula ina inagwanso ku **Mimosa ndi 38.2 mm, Thyolo Nchima 28 mm** komanso ku **Neno pa Boma 18.6 mm** (onani galafu pansipa). Kunazizira kwambiri m'sabatayi kunali ku **Dedza ndi 9°C** pamene ku **Kamuzu International Airport kunazizira ndi 9.8°C** pa 26 August. Pofika pa 1 September kazizilidwe kanatsikanso ndipo kwa Bvumbwe inafika **11.2°C** komanso ku Chichiri ndi **12.4 °C**.




## MALANGIZO M'SABATAYI

- Tisadzalowe panyanja pomwe mphepo ya Mwera ikuomba kuopa kutaya miyoyo ndi katundu.

## UNDUNA WA ZACHILENGEDWE NDI KUSINTHA KWA NYENGO

### NTHAMBI YOWONA ZANYENGO NDI KUSINTHA KWA NYENGO

- Tivale zovala zozitetezera ku nyengo yozizira kukamazizira makamaka ana and okalamba, komanso odwala mphumu (Asthma).
- Tipitirize kutsatira mwachidwi ndi kugwiritsa ntchito mauthenga a zanyengo.
- ***Kuti mudziwe zambiri funsani kwa:*** *The Director, Department of Climate Change and Meteorological Services, Ministry of Natural Resources and Climate Change, P. O. Box 1808, Blantyre, Malawi. Tel: (265) 882 266 579; Email: metdept@metmalawi.gov.mw , Website: www.metmalawi.gov.mw*

**Malo osindikizira: Blantyre** **Yatulutsidwa Lamulungu pa 1 September, 2024**